



KUPUNZIRA
kumachitika
kulikonde, nthawi
iliyonse nakuli
aliyense



Kupunzira kunyumba

Nanga chithunzi ichi ndicha ndani?

- Chithunzi ichi ndicha **mabanja onse** ali na ana olemala na osalemala.
- Ndi cha aliyense – amayi ndi abambo, osamalira, ana, achinyamata, abale, agogo ndi ambuya, amalume ndi azakhali ...

Nanga chithunzi ichi ndicha chiyani?

Chimankala chovuta ngati masukulu banavala komanso ana ali panyumba. Bakulu bamafuna kuthandiza ana ndi achinyamata kuti apunzire mwamene apunzirira ku sukulu, koma nichovuta.

Chithunzi ichi chikuwonetsa njira zambiri mabanja akupunzirira kudala kunyumba. Aliyense akonza kugwiritsa nchito malingaliro ake nakupanga zina njira izi zopunzirira.

Nanga nichiyani chitunzi ichi chinapangidwa?

Chithunzi ichi chitandiza mabanja kudziba mwamene kupunzira kumachitika kunyumba na mwamene **kupunzira kunyumba kungatandizire** kusintha kupunzira kusukulu na mderia.

Mwamene mungagwiritsire nchito chitunzi ichi?

- Ikani chithunzi ichi pakhoma lanu kuti aliyense mubanja azikwanisa kuchiwona. Funsani ana kuti atandizire kusanka pamene mungayike chitunzi ichi.
- Yanganani pa chitunzi ichi ntawi iliyonse.
- Ganizirani za zitunzi izi. Niziti zitunzi zamene mumakonda kuyangana kwambiri?
- Mwawona chiyani? Muganiza kuti nichani chamene chichitika muzitunzi izi?
- Chimupasani malingaliro bwanji wopunzirira kunyumba?
- Palibe mayanko yabwino kapena yoyipa.

Zinthu zofunika kukumbukira ngati mupunzirira kunyumba

Kupunzira kumachitika nthawi iliyonse **TIKAMVERANA** wina ndi mzake na umoyo wotizungulira...

- Kumvetsera kumachitika pakati pa aliyense. Bakulu bamamvera ana, ana bamamvera bakulu, bakulu bamamvera bakulu ndipo ana bamamvera ana.
- Pempani tandizo ngati kuli chamene simunamvere. Aliyense anga mutandizeni.
- Kambani nkani pogwiritsa nchito manja ndi nkhope. Onetsetsani kuti aliyense akhoza kumuwonani pokamba nkani.
- Mverani ku umoyo wokuzungulirani – mbalame, nyama, mvula. Yesani kupanga mawu yopalana.

Kupunzira kumachitika nthawi iliyonse ngati **TISOWERA** komanso **TIMASANGALALA** kunkala teka komanso ndi anzatu ...

- Tsiku lilonse, muziyendayenda m'njira iliyonse yamene mufuna. Kuvina. Kulumpha. Kugudubuza pansi.
- Sinthani masewera kuti aliyense alobemo. Ichi chitantaiza kusintha malamulo kapena kusintha mayendedwe amasewera.
- Pangani masewera atsopano ndikupunzitsa ena mwamene angasewerere.
- Mukankala mweka, munga puzye kapena kutanganidwa kutengera mwamene muzimvera.

Kupunzira kumachitika nthawi iliyonse **TIKAFUNA KUDZIWA** komanso kuti **TIDZIWE** zambiri za ife ndi anzatu ...

- Yetsani kuchita zinthu zatsopano, olo ziwoneka zovuta poyamba.
- Punzirani kuli wina na munzake. Pezani winangu wamene angamupunzitseni zamene mufuna kupunzira.
- Kulitsani chakuda. Samalirani mitengo. Konzani cinthu. Pangani china. Sinthani china. Funsani mafuso: Nanga izi zimachitika bwanji? Nanga ichi chimagwira ntchito bwanji? Chingachitike ndi chiyani ndikasintha izi?

Kupunzira kumachitika nthawi iliyonse **TIMAYAMBITSA** ndi **KUPANGA china chilichonse pogwiritsa nchito chilichonse chamene chili pafupi...**

- Gwiritsani nchito zinthu zilizonse zamene muli nazo kuzungulira, ngati mabotolo yakudala, mapaketi, tumutengo na matope kuti mupange zinthu zambiri zosiyanasiyana. Chilichonse munga gwiritsa nchito kumutandizani kuti mupunzire.
- Gwiritsani nchito kulingalira kwanu na zamene mumapeza kuti mupange nkhanzi. Nkhani zinga nkale 'zenizeni' kapena 'zongopeka'.
- Yesererani nkani zamene mumaganizira mumutu. Uzani banzanu zamene mwapanga. Kambani nkhanzi!
- Jubani zilembo kuchokera pampakete yakudala nakupanga mawu.

Kupunzira kumachitika nthawi iliyonse tikankala **BWINO** komanso **OKONDEDWA** olo tangena muzoruta ...

- Kumvera bwino komanso okondedwa ndiye maziko opunzirira ndi kukula. Ngati kulibe kuzimvera bwino komanso okondedwa chimankala chovuta kuti aliyense apunzire.
- Muyenera kusamalirana ndi kuthandizana. Khalani okomerana mtima wina ndi munzake, makamaka munthawi yamavuto.
- Chisamaliro chimachitika pakati pa aliyense. Bakulu bamasamalira ana, ana bamasamalira bakulu, bakulu bamasamalira bakulu ndipo ana bamasamalira ana.
- Aliyense amapunzira kuchokera ndikutengera zamene bamachita anthu owazungulira. Sonyezani mikhalidwe yamene mufuna kuwona.